The Baptist Tabernacle of Los Angeles

Mailing Address:
P. O. Box 15308
Los Angeles, CA 90015
Phone: (213) 744-9999
E-mail: rlhymersjr@sbcglobal.net
www.sermonsfortheworld.com
www.baptisttabernacle.com

Jack Ngann
Pastor

Dr. R. L. Hymers, Jr.
Pastor Emeritus

Disembala, 2021

Okondedwa anzanga:

Ndi wokula bwanji mayesero amene tikukumana nao, ndipo ndiwokula bwanji ubwino wa Mulungu! Chaka chino mu Januwale mkazi wanga wokondedwa Ileana anapezeka ndi kachilombo ka kolona. Ndinkaganiza kuti akufa. Mpingo wathu anamupempherera kwa nthawi zambiri. Ndipo azibusa ndi aKristu ambiri padziko lonse la pansi amamupempherera ndikumamutumizira ma uthenga a mafuno abwino. Mlaliki wina wa ku Pakistan ankamuyimbira foni m'mawa wina uliwonse! Mulungu anayankha, ndikumuchiza mkazi wanga kwa thunthu! Ndithokoze onse amene anatengapo mbali pa kumupempherera.

Vesi langa la pa mtima lakhala liri Afilipo 4:13. Ndipereka pamodzi ndi vesi lomwe liri patsogolopa. Baibulo limati,

> "Ndadziwa ngakhale kupeputsidwa, ndadziwanso kusefukira; konseko ndi m'zinthu zonse ndalowa mwambo wa kukhuta, ndiponso wakumva njala; wakusefukira, ndiponso wa kusowa. Ndikhoza zonse mwa Iye wondipatsa mphamvuyo." (Afilipi 4:12,13)

Kristu anandirimbikitsa ine ndi Ileana mu nthawi ya matenda ake. Ndiponso Kristu akutirimbikitsa pamene tikusangalala ndi kuthokoza Mulungu chifukwa cha machiritso ake. "Ndikhoza zonse mwa Iye wondipatsa mphamvuyo."

Pa Marichi 24 otsatsa malonda anagulitsa nyumba yathu ya kale yomwe iri mkati mwa mzinda wa Los Angeles. Tsopano akuyigwiritsa ntchito ndi a tchalitchi cha chi Korea. Ndalama zake zikugwiritsidwa ntchito pokonzanso nyumba yathu yatsopano yomwe iri ku San Gabriel. Jack Ngann ndi amene akhale mbusa wa mpingo watsopanowu, "Mpingo wa Baptist wa chi China wa chihema cha ku Los Angeles."

Pa Epulo 11 tonse tidasonkhana ku Beverly Hilton Hotel kusangalalira tsiku langa lobadwa la chi 80, chomwe chinachitika tsiku lotsatira lake. Mafuno abwino anafika kuchokera kwa a laliki ndi a Kristu kuchoka kudziko lonse la pansi. Mwana wathu Robert Leslie analipira zakudya zonse ndi zonse zokhudza phwando limenero. Robert ndi mwana wa nzeru komanso wochita bwino pa chuma. Mbusa Ruperto Medina, mbusa wa Bethesda Christian Church omwe uli ku dziko la Dominican, anabwera kuno pa ndege kudzangopemphera pemphero lotsekulira mwambowu. Tinali ndi nthawi yopambana kwambiri!

MUTHA KUWERENGA ZIKWI-ZIKWI ZA MA ULALIKI A MAU-KU-MAU NDI ZIPHUNZITSO MU ZILANKHULO MAKUMI ANAYI NDI MPHAMBU ZISANU NDI CHIMODZI PA WWW.SERMONSFORTHEWORLD.COM.

Pa Meyi 3 ulaliki mchi Odia unapezeka pa tsamba lathu la www.sermonsfortheworld.com. Odia ndi chimodzi mwa zilankhulo zambiri zopezeka ku India. Anthu oposa 30 miliyono amalankhula chilankhulochi ngati chilankhulo chao choyamba! Sindilipiritsa kuti anthu amvere maulaliki amenewa. Chikhumbo-khumbo changa ndi chakuti anthu aupeze Uthenga wa bwino padziko lonse la pansi mzilankhulo zochuluka. Ndichifukwa chake ma ulaliki amenewa sioletsedwa kuagwiritsa ntchito, anthu akhoza kuagwiritsa ntchito mnjira ina iri yonse angafunire. Sabata ina iriyonse timalandira ma email kuchoka pa dziko lonse la pansi kundithokoza pakuthandizira kuti ma uthengawa azipezeka.

Pa Meyi 14 chinthu cha chikulu chinachitika. Mdzukulu wathu Robert Leslie Hymers IV anabadwa! Ndi mwana wa mwamuna wa mwana wanga Robert ndi mkazi wake Jin. Alinso ndi ana awiri akazi, Hannah ndi Sarah. Kakhanda ka tsopanoka ndi mdzukulu wathu woyamba komanso yekhayo wamwamuna. Ndimamutcha kuti "Mfana Bob." Ndikooneka bwino zedi, ndipo ndikupemphera kuti Mulungu adzamuitana kukhala mlaliki!

Kristu wandirimbikitsa m'thawi za bwino komanso zoyipa, pamene ndi wokhuta komanso pamene ndiri ndi njala, pamene ndiri ndi zochuluka ndi pamene ndisowa. Mu mwezi wa Juni ndinafa ziwalo. Kuyambira pamenepo ndimangopumula ku nyumba. Ndiri ndi munthu amene amandithangatira, wodziwa ntchito yake bwino, koma wothangatira wa mphamvu kwambiri ndi mkazi wanga Ileana. Zingavute maka, sindidzasiya kularika Uthenga wabwino. Sabata iriyonse ndimajambula uthenga pa kanema umene umaonetsedwa ku tchalitchi lathu ndi kuikidwa pa tsamba lathu la itaneti. M'moyo wanga wonse, Kristu amandirimbikitsa!

Ndakhala ndi kuuza mpingo wanga nkhani ya Marilyn Frarnik. Kale kwambiri akanali mtsikana wa chichepere amakha mdziko la Marin, kumpoto kwa mzinda wa San Francisco. Marilyn amadalira Yesu. Amai ake amafunitsitsa ngati Marilyn akadamatenga mankhwala o zunguza bongo komanso atamangochita za chisembwere ndi anyamata. Amayi akewo analibe gawo liri lonse ndi za Kristu! Anamuthamangitsa Marilyn panyumba pao. Marilyn anayimabe chiimire pa chikhulupiriro cha pa mpulumutsi. Ndi mwamuna wake Jerry, iye ndi wa mishoni ku dziko la Czech. Pa Augusti 26 Jerry ndi Marilyn anabwera kunyumba kwathu kudzandiyendera. Analankhulapo za utumiki wao umene tinaujambula pa kanema ndi kuuonetsa ku mpingo. Ndi mdalitso kwambiri! Ndipo ndikokoma Kotani kuona chisomo cha Mulungu chikupulumutsa anthu ndiku chigwiritsa ntchito pa utumiki. Ngati mtumwi Yohane anati, "Ndiribe chondisangalatsa kwambiri koposa kumva kuti ana anga akuyenda mchoonadi" (III Yohane 4).

Pa Augusti 29 Jack Ngann anasonyezedwa ku mpingo ngati mbusa wathu watsopano. Jack ndi mu Amereka koma ndi wa chi China. Anakwatira ndipo ndi bambo wa ana awiri. Ine mbusa Emeritus, amene ndinamuphunzitsa ntchito ya ubusa, mbusa wanga Dr. Timothy Lin ndi amene anandiphunzitsa. Mbale Ngann ndi m'Kristu wa mphamvu ndipo tiri ndi chiyembekezo chachikulu mwa iye. Chonde pempherani mpingo wanu wa tsopano ndi utumiki wake kumeneko.

Pa Septembala 22 ntchito yokonzanso tchiritchi chathu chatsopano ku San Gabriel inayambika. Nyumbayi idzayamba kugwiritsidwa ntchito kumayambiriro a chaka cha mawa. Chiri pakati pa anthu a chi China ambiri.

Mu Okutobala bambo ake a Ileana a Rafael Cuellar anauluka pa ndege kuchoka ku Guatemala ndi kudzakhala nafe m'nyumba mwathu kwa ma sabata angapo. Ndi munthu wa ulemu wake, komanso wochangamuka ndi wa machawi- choti mudziwe china ndi chakuti ali ndi zaka zoposa 90. Tinkasangalala kuti wakwanitsa zaka 91 m'nyumba mwathu ndi mpingo pa Okutobala 29.

Pa Novembala 21 tidali ndi nthawi yabwino ya phwando lothokoza ndi mpingo wonse mnyumba mwathu. Zakudya zokhetsa duvu zidaphikidwa bwino ndithu! Tikuthokoza Ileana, Jack Ngann, ndi a dikoni athu a Mencia potiphikira zakudya ndi chikonzero chonse.

MUTHA KUWERENGA ZIKWI-ZIKWI ZA MA ULALIKI A MAU-KU-MAU NDI ZIPHUNZITSO MU ZILANKHULO MAKUMI ANAYI NDI MPHAMBU ZISANU NDI CHIMODZI PA WWW.SERMONSFORTHEWORLD.COM.

Ichi chinali chaka chopambana! Ulemerelo wonse upite kwa Mulungu amene anayankha ma pemphero athu ndi Kristu amene anapulumutsa miyoyo yathu. Ndimakumbukira mau amene George Beverly anayimba pa msonkhano wa chitsitsimutso wa Billy Graham wa mchaka cha 1991 ku Glasgow, mdziko la Scotland,

> Zikomo, Atate, Potipatsa mwana wanu
> Ndi posiya Mzimu wanu 'Mpaka ntchito yanu itamalizika'.
> ("Kuli Mpulumutsi" ndi Keith Green, 1953-1982).

Pamene tikusangala kuti kwabadwa mpulumutsi tiyeni tifuule, "Zikomo Ambuye Mulungu. Ndipo Yesu Kristu alemekezedwe!"

Ine ndiri pakati pa mzere wa patsogolo ndi mdzukulu wanga Hannah kumanzere ndi Sarah kumanja. Mzere wa kumbuyo, Kuchoka ku manzere kupita ku manja: Bambo a Ileana Rafael Cuellar, mai a Ileana Linda, mkazi wa Robert Leslie Jin, mfana Bob atanyamullidwa ndi bambo ake Robert, mkazi wanga Ileana, mwana wathu Wesley ndi mchemwali wa Ileana, Yvette Cuellar.

Ine wanu mdzina la Yesu,

Mbusa. R. L. Hymers, Jr.,
D.Min., D.Rel., Th.D., Litt.D.
Afilipo 4:13

MUTHA KUWERENGA ZIKWI-ZIKWI ZA MA ULALIKI A MAU-KU-MAU NDI ZIPHUNZITSO MU ZILANKHULO MAKUMI ANAYI NDI MPHAMBU ZISANU NDI CHIMODZI PA WWW.SERMONSFORTHEWORLD.COM.